Kodi Yesu Khristu Ndi Ndani? (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 4 m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI YESU ANANGOKHALA MUNTHU WABWINO BASI?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti ayi?

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti inde?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

N’zofunika kudziwa zoona zokhudza Yesu.

(Werengani mutu 4 m’buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1 mpaka 3.)

Werengani Yohane 17:3.

Kodi vesili likusonyeza kuti ‘kuphunzira ndi kudziwa’ za Yesu (ndi Atate ake) kungatithandize bwanji?

Werengani Yohane 14:6.

Kodi n’zotheka kupeza moyo wosatha popanda kudziwa Yesu molondola?
Ngati mukuti ayi, fotokozani chifukwa chake komanso ngati mukuti inde fotokozaninso chifukwa chake.

Zimene zinafotokozedwa m’Baibulo zokhudza Mesiya zimatithandiza kumuzindikira mofanana ndi mmene chithunzi chingatithandizire kuzindikira munthu amene sitinamuonepo

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Mulungu anatumiza Yesu padziko lapansi kuti adzakhale Mesiya wolonjezedwa.

(Werengani mutu 4 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 4 mpaka 9.)

Werengani Mika 5:2 ndi Mateyu 2:1, 3-6.

Kodi kubadwa kwa Yesu kunakwaniritsa bwanji ulosi wonena za Wolonjezedwa?

Werengani Mateyu 3:16, 17 ndi Yohane 1:32-34.

N'chiyani chinathandiza Yohane M'batizi kukhulupirira kuti Yesu anatumizidwadi ndi Mulungu?

N'chiyani chimakupangitsani kukhulupirira kuti Yesu ndi Mesiya wolonjezedwa?

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

Yesu anangokhala munthu wabwino yemwe anakhala padzikoli kale kwambiri.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti Yesu anali munthu wabwino. Koma ndimakhulupirira kuti analinso ndi udindo wapadera chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Yesu sanali Mesiya. Ankangochita zinthu pofuna kudzionetsera ngati Mesiya.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Anthu ambiri angakhalenso ndi maganizo amenewo. Koma tiyeni tione chinthu china chimene Yesu sakanangochita yekha popanda kuthandizidwa ndi Mulungu . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania